

CHIKONZERO CHACHIDULE CHA MULUNGU CHA CHIPULUMUTSO

Mzanga,

Ndiri kukufunsani funso lofunika kwambiri la moyo. Chimwemwe ndi madandaulo nthawi zonse agonera pa yankho lanu. Funso ndi lakuti: Kodi mudapulumsidwa? Funsoli silikuti ndinu abwino chotani, kapena ndinu membala wampingo, koma mudapulumsidwa? Kodi muli kutsimikiza kuti mudzapita kumwamba mukadzafa?

Mulungu akunena kuti, popita kumwamba muyenera kubadwanso. Mu Yohane 3:7, Yesu anati kwa Nekodemo, **“Uyenera kubadwa kwatsopano.”**

Mu Baibulo, Mulungu watipatsa ife chikonzero cha m'mene tingabadwire kwatsopano kumene kutanthauza kupulumutsidwa. Chikonzero chake ndi chosavuta! Mungathe kupulumutsidwa lero. Motani?

Choyambirira, mzanga, muyenera kuzindikira kuti ndinu wochimwa. **“Pakuti onse anachimwa, naprewera pa Ulemelero waMulungu.”** (Aroma 3:23).

Chifukwa ndinu wochimwa, mwaweruzidwa ku imfa. **“Pakuti mphoto [malipiro] yache ya uchimo ndi imfa”** (Aroma 6:23). **Uku ndiko kulekana ndi Mulungu wa m'gehena.**

“Ndipo popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa, chiweruziro.” (Ahebri 9:27).

Koma Mulungu anakukondani kwambiri Iye anapatsa Mwana wache wobadwa yekha. Yesu, kusenza machimo anu ndi kufa m'malo mwa inu “ ... Anamyesera [*Yesu amene sanadziwe uchimo*] uchimo m'malo mwathu; kuti ife **tikhale chilungamo cha Mulungu mwa Iye**” (2 Akorinto 5:21).

Yesu anayenera kukhetsa mwazi wache ndi kufa “Pakuti moyo **wa nyama** ukhala m' mwazi” (Levitiko 17:11) **“Wopanda kukhetsa mwazi kulibe kumasuka [kukhululukidwa]”** (Ahebri 9:22).

“Koma Mulungu atsimikiza kwa ife chikondi chache cha mwini yekha m'menemo, kuti pokhala ife chikhalire wochimwa, Khristu adatifera (Aroma 5:8).

Ngakhale kuti sitimavetsetsa m'mene, Mulungu adanenera kuti machimo anga ndi machimo anu adasenzedwera pa Yesu ndi kufa m'malo mwathu. Adakhala wotilowera m'malo mwathu. Ndi zoonza Mulungu sanganame.

Mzanga; **“Mulungu ... koma tsopano alinkulamulira anthu onse ponse ponse atembenuke mtima”** (Machitidwe 17:30).

Kulapa uku ndiko kusinthika kwa moyo umene ugwirizana ndi Mulungu kuti m'modziyo ndi wochimwa, ndiponso kugwirizana ndi zimene Yesu adachita kwa ife pamtanda.

M'Machitidwe 16:30-31, Mdindo wa ndende wa ku Filipi anafunsa Paulo ndi Sila: **“ ... Ndichitenji kuti ndipulumuke?” Ndipo iwo anati, ukhulupirire Ambuye Yesu udzapulumuka...”**

Mwachidule khulupirirani Iye monga m'modzi adasenza machimo anu, ndikufa m'malo mwanu, amene Mulungu adamuukitsa kwa akufa.

Kuuka kwache mwamphamvu kutsimikiza kuti wokhulupirira ali nawo moyo wosatha, pamene Yesu alandilidwa monga Mpulumutsi.

“Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana aMulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lache” (Yohane 1:12).

“Pakuti, amene ali yense adzaitana padzina la Ambuye adzapulumuka” (Aroma 10:13).

Ali yense kuphatikizapo inuyo. Adzapulumuka sikutanthauza kuti mwina, kapena, koma adzapulumuka. Zoonadi, muyenera kuzindikira kuti ndinu wochimwa. Tsopano lino, kuli konse kumene muli, mulape, ukwezeni mtima wanu kwa Mulungu mu pemphero.

Mu Luka 18:13, **wochimwa adapemphera:** “Mulungu ndichitireni chifundo ndine wochimwa”. Mungopemphera: *“Ho! Mulungu mundichitire chifundo, ine wochimwa. Ndikhulupirira mwazi wache wokhetsedwa, imfa, kuikidwa m 'manda kwache ndikuuka kwache kuti zonse zinachitika chifukwa cha ine. Ine tsopano ndikumlandira Iye monga Mpulumutsi wanga. Ndikuyamikani chifukwa chondikhululukira machimo anga, mphatso ya chipulumutso ndi moyo wosatha, chifukwa cha chifundo chachisomo chanu.”*

Mutengeni Mulungu M'Mau ache ndi kupempha chipulumutso mwa chikhulupiriro. Kbulupirirani ndipo mudzapulumuka. sim'pingo, simalo ogonako, sintchito zabwino zimene zingakupulumutseni. Kumbukirani. Mulungu ndiye amapulumsa. Zonse za izi.

Chikonzero chachidule cha Mulungu cha chipulumutso ndi: Ndinu wochimwa. Choncho, pokba pokba mutakhulupirira Yesu amene adafa m'malo anu, mudzakhala nthawi zonse mugehena. Ngati mukhulupirira Iye monga wopachikidwa wanu, woikidwa m'manda ndi Mpulumutsi wouka; mulandira chikhululukiro cha machimo anu onse ndi mphatso ya chipulumutso chosatha mwa chikhulupiriro.

Mukuti, “Zoonadi, sizingathe kukhala zovuta. “Inde ndi zosavuta. Ndi Malemba. Ndi chikonzero cha Mulungu. Mzanga. khulupirirani Yesu ndi kumulandira Ive monga Mpulumutsi lero.

Ngati chikonzero chake sichikumveka bwino bwino werengani mobwereza. bwereza kathilakika, musanakasiye pansi mpaka mutakamvetsetsa. Moyo wanu uli wofunika kuposa dziko lonse lapansi. “**Pakuti munthu apindulanji akadzilemezera dziko lonse, natayapo moyo wache?**” (Marko 8:36).

Mutsimikizedi kuti mwapulumsidwa. Ngati muutaya moyo wanu, musemphana nako kumwamba ndipo mwataya zonse. Chonde, muloleni Mulungu akupulumutseni nthawi ino.

Mphamvu ya Mulungu idzakupulumutsani, kukusungani wopulumuka ndi kukupangani inu kukhala m'chigonjetso cha moyo wa Chikristu. “Sichinakugwerani inu chiyeso koma cha umunthu; koma Mulungu ali wokhulupirika, amene sadzalola inu kuyesedwa koposa kumene mukhoza: koma pamodzi ndi chiyeso adzaikanso populumukirapo, kuti mudzakhokekupirira, amene sadzalola inu kuyesedwa koposa kumene mukhoza: koma pamodzi ndi chiyeso adzaikanso populumukirapo, kuti mudzakhoke kupirirako.” (I Akorinto 10:13).

Musakhulupirire zolinga zanu. Zidzasinthika. Imani pamalonjezo aMulungu. Sasinthika. Mutatha kupulumutsidwa, pali zinthu zitatu zochita tsiku lili lonse kuti mukule mumzimu: Pempheerani - Mumalankhula kwa Mulungu. Werengani Baibulo lanu - Mulungu alankhula kwa inu. Chitirani Umboni - Mulankhule za Mulungu.

Mubatizidwe kumvera Ambuye Yesu Khristu kukhala umboni wa poyera wa chipulumutso chanu, ndipo muphatikane nawo ampingo umene ukhulupirira Baibulo mosachedwa. “**Potero usachite manyazi pa umboni wa Ambuye wathu ...**” (2 Timoteo 1:8).

“Chifukwa chache yense amene adzabvomereza [kuchita umboni] Ine pamaso pa anthu, Inenso ndidzabvomereza iye pamaso pa Atate wanga wa kumwamba” (Mateyu 10:32).